KIDStory®
A PROGRAM OF KIDS AROUND THE WORLD

## Kutsegulila

- Sankhani funso kapena masewela omwe ana angachite kuti agawile nkhani zawo.
- Yankho lanu liyenela kupatsa chidwi ana.
- Funsani funso lomwe yankho lake liyenela kukhala 'eya' kapena 'ayi'.

Mau otsegulila asachite kukhala ochokela mu baibulo mokha koma awapangitse ana kuganiza molunjika ku kaganizidwe kao

## Maziko:

- Tchulani mau kapena fotokozani madela ndi zikhalidwe zosiyanasiyana zimene ana angalephele kuzidziwa.
- Fotokozani zochitika zofunika,zomwe zachitika mutsiku la lero.
- Ngati pali kofunikila abwelezetseni nkhani za kale.

Simukufuna kulelekeze pakati pankhani kuti mufotokoze mau motelo onetsetsani kuti mwafotokoza musanayambe

## Nenani nkhani:

- Phwanyani nkhani m'magawo anaiyi kapena asanu.
- Aloleni ana atenge nawo mbali.
- Gwilitsani ntchito zisudzo zomwe zingapangitse nkhaniyi kukhala yochititsa chidwi.gwilitsani ntchito zinthunzi zooneka ndimaso kuonetsa mmagulu
- Onetsetsani kuti nkhani ndiyayifupi kuti ana atha kuphunzila komaso kuuza anzao.

Nenani nkhani mmene ilili. Musaonjezele mau kapena kuchotsela mau.

Ipangeni yachikumbutso koma mukhala muchoonadi chamawu amulungu.

Ndizofunika kuti ana adziwe nkhani za m'baibulo komaso kudziwa kuti ndizoona.

## kufotokozaso:

- Ana akhale nao ma baibulo komaso awelenge nkhani ndikubwelezanso.
- Sankhani masewelo kapena zochitika zomwe ana atatenge nao mbali.

Onetsetsani kuti anao akufotokoza nkhani zolondola za m'baibulo.

## Pezani ndi kuyankha mafunso:

- Pemphelani mphunzilo molingana ndi mmene mzimu oyela ungakutsogoleleni pazokambilana zanu.
- Gwilitsani ntchito mafuso ochokela muntima osati mmutu mwano.

Apangitseni ana kukumbukila mfundo za zomwe mulungu akuwachitila mmiyoyo yao komaso mmitima yao munkhaniyi.

Tikufuna mzimu uyankhule mau opeleka tanthauzo pa moyo wa munthu

# Zitsanzo

## Nenani nkhani:

- Gwilitsani ntchito chovala kapena chida.
- Lolani ana apange phokoso (kutikita manja kuti apange phokoso ngati la mvula).
- Yendani mozungulila muchipindamo. Gwilitsani ntchito nkhope yanu pofotokoza.
- Nenani nkhaniyo mwa inu nokha (ngati ndinu mmodzi mwa anthu ali munkhaniyo).

## Kufotokozaso:

- Masewelo: Mipando ya nyimbo. Munthu aimilile ndikufotokoza gawo loyamba la nkhani. Bwelezani nkhani kufikila mutamaliza.
- Zisudzo: Chikwangwani. Semani chikwangwani chofotokozela nkhani.
- sewelo: Apatseni ana chida ndipo muonenelele mmene iwo angachigwilitsile ntchito pofotokoza nkhani.
- Nyimbo: Pekani nyimbo yamutu wankhaniwo.
- Kulemba: zotsatila. Aloleni ana alembe zomwe mulungu akufuna iwo atachita ndi zomwe ali nazo

## Pezani ndi Kuyankha mafunso:

***Mfunso lamutu(****mfundo)*

- ndichani chomwe chadziwika munkhaniyi?
- Mungaganizile muli mmenemo? Mwamva/mwaona/mwanunkhiza/mwakhudzidwa ndi chani?
- Mulungu/Yesu akuwaphunzitsa chani munkhaniyo?
- Mulungu/yesu wayankha motani?
- Anthu akusiyana kapena kufanana bwanji munkhaniyi?

***Mfunso lamtima***(kumverera)

- Mukuganiza kuti chaphindu ndi chani mu nkhani ya tsiku la lero?
- Mumamva bwanji mmene mumamva za nkhaniyi?
- Mukuganiza chimachitika ndi chani mu mtima ndi mmalingalilo a ________ munkhaniyi?
- Mukumva bwanji za mulungu/yesu?
- Mukugani ndichifukwa chani Mulungu/yesu Anaika nkhaniyi mu baibulo?

***Funso la dzanja***

*(kuchitapo kanthu)*

- Mwatolapo chani lero chomwe chitha kukupangitsani kusintha moyo wanu?
- Mutatha kumva nkhaniyi mwakhala bwanji mu moyo osinthika?
- Munsabatayi mungagawane ndi ndani zankhaniyi?
- Mchifukwa chani mulungu amafuna kuti mumve nkhani yake?